

Mopangira ndi kugwiritsa nchito Zowolera



Implemented by



In cooperation with



Kasisi Agriculture Training Centre (KATC) is an in-country partner of the Knowledge Hub for Organic Agriculture and Agroecology in Southern Africa (KHSa). KHSa is part of the Knowledge Centre for Organic Agriculture and Agroecology in Africa (KCOA), a collaborative country-led partnership funded by the German Federal Ministry of Economic Cooperation and Development (BMZ) and implemented by the Deutsche Gesellschaft für Internationale Zusammenarbeit (GIZ) GmbH and non-governmental organisations across Africa. The KCOA aims to scale up the adoption of agroecological and organic farming practices through five knowledge hubs in Africa. The other hubs are implemented by GIZ with in-country partners in North, West, East and Central Africa. KHSa partners with KATC and PELLUM Zambia in Zambia, the Namibian Organic Association and Namibia Nature Foundation in Namibia, Soils, Food and Healthy Communities and the Kusamala Institute of Agriculture and Ecology in Malawi and the South African Organic Sector Organisation and Participatory Guarantee Systems South Africa in South Africa. Implementation is supported by the South African-based Sustainability Institute.

Zowolera ndi ciani?

Iyi ndi fataleza wa cilengedwe wopangidwa poyala mwa ndondomeko, zipangizo monga zokhalira mutakolola, tsekela, zotsala ku ndiwo za m'madimba (kucokera ku khitchini) ndi manyowa. Izi zizayamba kuphikika ndi kutentha ndipo zizawola. Mulu wa zowolera umasandulizidwa kuthandizira kuti ziwole ndipo zikakonzeka zimaoneka zakuda bii. Sakanizani izi ku nthaka kuti ikhale ya conde.

Zofunikira

- ▶ Masaka 20 azipangizo zofiira monga: tsekela, zikopa, mapesi, gaga wampungwa, matsambaouma.
- ▶ Masaka 5 a zipangizo za mutundu wa msipu [monga zingapezekere]: zomerela, zotsalaza ndiwo zam' madimba monga zikamba, udzu wa msipu ndi masamba a mbewu zopeleka choonde.
- ▶ Saka limodzi la manyowa aziweto.
- ▶ Madzi kucitira kuti tizilombo tizikhala tamoyo. Utu nditwatung' ono kwambiri tosaoneka ndi maso, koma tumawoletsa zipangizo. Tumankhalanso mu nthaka ndi kuithandizira kukhala lathanzi.
- ▶ Timitengo/mitsononkho.
- ▶ Dothi.

Musasewenzetse zipangizo izi

- ▶ Zomera zili ndi matenda kapena zapaizoni [monga mono].
- ▶ Zomera zimene zimacedwa kuwola.
- ▶ Zomera zizazamwitsa nthaka ndi zowononga (ngowe ndi bulugamu) kapena zomera zili ndi zoletsa kuwola (paini).
- ▶ Manyowa achona ndi agalu, amenewo angakhale ndi tizilombo toyipa.
- ▶ Mabonzo a nyama ndi zina zotsala kuzakudya za nyama cifukwa zimabweretsa akhoswe.
- ▶ Zosawola zilizonse zopangidwa ndi munthu: ma pulasitiki, ma galasi ndi malata.
- ▶ Zoopsya monga ma batili akutha, luwe ndi zinyalala za mankhwala.
- ▶ Zakudya za mafuta-mafuta.

SANKHANI NDI KUKONZA MALO



1

Sankhani ndi kukonza malo mu m'thunzi [munsi mwa mtengo], woyalidwa bwino, pafupi ndi zipangizo zofunika [manyowa a ziweto, zokhalira pokolola, madzi]. Ngati n'kotheke, kufupi ndi munda komwe zipita. Izi zicepetsa nthawi ndi zobvuta.

LEMBANI MALO NDI KUIKA MPHOMPHO



2

Pimani ndi kuzindikira ukula kwa muulu. Ikani mphompho zitali-zitali mngodya zinai za muulu. Ukula kwabwino kwa muulu ndi 1m m'camimba ndipo pakati pa 1m ndi 1.5m mkuima. Kuculuka kwa zipangizo kuzalamula utali wake mcogona.

YALANI ZIPANGIZO ZA MAZIKO



3

Ikani zinthu zosanjikiza kapena zosanjikizana monga zitsononkho, timitengo ndi mapesi pansi. Izi zitalikire 20cm ca m'mwamba.

WONJEZERANI ZIPANGIZO ZOFIIRA



4

Wonjezerani wosanjikiza wotalika 20cm ca m'mwamba wa zofiilira monga tsekera, masamba ouma kapena gaga wa mpunga.

WAZANI MADZI PA MUULU



5

Muziwaza madzi pa muulu pambuyo poika zipangizo zofiira.

YALANI ZIPANGIZO ZA MSIPU



6

Yalani zipangizo zotalika 10cm ca m'mwamba za msipu makamaka masamba a mbeu monga nyemba, kaela ndi chitedze. Mungawonjezere zotaya zaku kitchini [makoko a ndiwo za n'thilira kapena za masamba zowola] kapena udzu.

YALANI MANYOWA



7

Sanjikizani manyowa. Ku manyowa ndiye kucokera nayitrogeni wa mulu wa zowolera. Manyowa afunika kuwazidwa mpaka pakati pa 2cm kufikira 5cm ca m'mwamba. Onjezerani zowolera kapena nthaka ngati muli nazo. Ici ciwonjezera tizilombo topangitsa kuti ziwole mwamsanga.

PITIRIZANI KUYALA ZIPANGIZO



8

Pitirizani kusanjikiza zipangizo. Wonjezerani zipangizo za zofiira, wazani madzi, yalani zipangizo za msipu, ndipo sanjikizani manyowa [kuwonjezera nthaka kapena zowola kale ngati muli nazo]. Muzibwerezazi koma mulu wanu usadutse 1.5m ca m'mwamba.

VINIKIRANI MUULU



9

Vinikirani muulu woose ndi udzu kapena zopuntha za mpunga kuutetedza ku dzuwa kapena mvula.

ONANI KUTENTHA



10

Jinyani kamtengo katali mopindika pa muulu ndikukasiya momwemo masiku 2/3. Ngati kamveka kutentha kakacotsedwa ndiye kuti muulu ukuwolera bwino.

SANDULIZANI MUULU



11

Ngati kamtengo katentha, musandulize muulu patapita masiku 7 kufika 10. Kusanduliza ndiko kubweretsa zamkati kunja, ndikupereka zakunja m'kati. Pakusanduliza, muziwaza madzi. Muziyesabe kutentha, ngati zitentha bwino, sandulizani pakapita masiku 7 kufikira 10 kufikira zitakonzeka zowolera.

12

KULONGOSOLA MUULU

Sandulizani muulu pomwepo ngati kamtengo ndi kotentha kwambiri kuti simungagwilirire mpindi 30. Siziwolera bwino ngati kamtengo sikatentha. Mungafunike kuwonjezera manyowa ena kapena/ndi madzi (ngati muulu ndiwowuma kwambiri).


ONANI NGATI ZOWOLERA ZAKONZEKA



13

Zowolera zikonzeka posanduliza kanai kapena patapita masabata 6 kufikira 8. Zowolera zikafikapo, zimveka ngati nthaka losetekera bwino ndikuoneka kuda bii mutazigwira. Musandulizenso ndikuzaona pakapita sabata limodzi ngati sizosetekera.

KUGWIRITSA NCHITO ZOWOLERA



14

Mungagwiritse zowolera m'njira zosiya-siyana. Ikani zowolera muyeso manja awiri mdzenje mudzabyala mbewu; kumbilani kumodzi ndi nthaka mu m'bedi muzabyala; kapena kuwaza mutsinde mwa zomera zokula kale. Ngati mwaika mu dzenje kapena mwawaza patsinde la zomera, vinikirani ndi dothi pang'ono.

© Kasisi Agricultural Training Centre, 2023

This knowledge product can be copied, reproduced, adapted, translated, used to make derivatives and disseminated for not-for-profit and/or educational purposes only. It cannot be used for commercial purposes in any way, shape or form. To access and understand the document's copyright policy as at 19 May 2023, use the QR code:

